

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

VALANI ZIDA ZONSE ZA MULUNGU

Tavalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kuchilimika pokana machenjerero a mdierekezi. — Aefeso 6:11

Mulungu anakonza kuti kudzera mwa Mwana wake Yesu Khristu ndiponso kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera ana ake akhale ndi moyo wopambana ndi waumulungu. Nkhondo yauzimu ikuwirira, ndipo miyoyo ikusokeretsedwa ndi kugonjetsedwa ndi mphamvu ya Mdierekezi. Akhristu ambiri akukhala mu mkhalidwe wauchimo ndi kulephera. Nkhani yabwino ya Uthenga Wabwino ndiyo yakuti mu nyengo inoyo Mulungu anakonza kuti tigonjetse uchimo ndikukhala ndi moyo wa chigonjetso ndi wa chisangalalo tsiku ndi tsiku.

Chinthu choonekeratu cha chigonjetso chimatanthauza kuti msilikali wamtanda akuyenera kuvala zida zonse za Mulungu, kuti akhale ndi mphamvu yokana ndi kugonjetsa chinyengo ndi mphamvu za Woipayo. Mulungu sanatisiye opanda chitetezo koma anatipatsa zida zotithandiza kuti tipite chitsogolo ndikukhala opambana pa mphamvu ZONSE za mdani.

Ngati msilikali wasiya chimodzi mwa zida zake kapena gawo lina la zida zake ndiponso sazinyamula popita kunkhondo, iye amakhala wosatetezeka ndipo samakhala ndi zida zokwanira zomenyera nkondo. Zimangotengera kuti msikilikalio akhale wosatetezeka kamodzi basi kuti agonjetsedwe. Izinso zili chimodzimodzimodzi ndi Mkhristu. Tikuyenera kugwiritsa ntchito mwai uliwonse umene Mulungu wapereka; ndipo potero, tidzatha KUKHALABE okhulupirika, oona, ndi opambana. Pa Aefeso 6:14-17 amatchula zida zonse za Mulungu.

Lamba wa Choonadi: Lamba wa msilikali wachiroma ankagwiriziza zida zankhondo

pamalo ake oyenera. Ndi choonadi cha Mau a Mulungu chenicheni, chogwirika, ndi chopanda malire chimene chidzatitsogolera motetezeka kupita Kumwamba. Mdierekezi ndi wabodza, ndipo akugwira ntchito m'dzikoli komanso m'nyumba zopemphereramo. Mau oyera a Mulungu ndi amene adzaulula chinyengo cha mdani ndi kupereka kuwala mumdima. Choonadi chonyengerera chimafooketsa Akhristu ndipo chimabweretsa kugonjetsedwa. Choonadi choyera chimabweretsa mphamvu ndi nyonga kwa woyera mtima wa Mulungu ndipo chimapereka zida polimbana ndi mabodza owononga a dziko lapansi ndi chipembedzo chonyenga.

Chovala cha pachifuwa cha Chilungamo:

Chida chankhondo chimenechi chinkateteza chifuwa ndi mtima wa msilikali. Chilungamo cha Khristu mwa ife ndi chimene chimateteza ndi kusunga moyo wathu wauzimu. Kupumula mu chilungamo cha Mulungu osati mu mphamvu zathu kumatithandiza kukhala oyera m'dziko lino losaopa Mulungu. Ndi Khristu, mwana wa Mulungu kenaka adzapanga zisankho zomwe zimalimbikitsa chitetezo chazimu komanso zomwe zidzamuteteze ku kudetsedwa kwa dziko lapansi. Asilikali a Khristu sangasiye chilungamo, chifukwa kupanda kutero adzagwidwa ndi uchimo. Pamene Akhristu ateteza mitima yao ndi maganizo ao ndi kukonda Mulungu ndi njira yake yopatulika kuposa china chilichonse, adzagonjetsa zilakolako za dziko lapansi.

Nsapato za Uthenga Wabwino wa

mtendere: Nsapato zinkateteza mapazi paulendo wautali. Kulikonse kumene Akhristu amayenda, amayenera kupita ndi mbiri yabwino ya uthenga wabwino. Yesu ndiye wopereka mtendere ndipo mtenderewo uyenera kukuta ndi kudzaza mitima yathu. Komanso, ana a Mulungu ayenera

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Mu nyengo inoyo Mulungu anakonza kuti tigonjetse uchimo ndikukhala ndi moyo wa chigonjetso ndi wa chisangalalo tsiku ndi tsiku.”

Mau a Mkonzi

Kalozera posanthula
Baibulo

Moyo Wachikhristu
Wopambana

Mafunso Mayankho

Kodi Mukudziwa?

Mau a Nyengo Yake

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

kufunafuna mtendere m'kuyanjana kwao onse ndi anthu. Maubale oononga apangitsa kuti Akhristu ambiri agwe. Valani ku mapazi kwanu ndi uthenga wabwino wa mtendere ndi kutsata chiyanjano osati mikangano ndi kuyambana ndi banja lanu ndi anansi anu.

Chishango cha chikhulupiriro: Chishango cha msilikali wachiroma chinali chachitali kuposa msinkhu wake kawiri. Chimapereka chitetezo kwa msilikali ku mivi ndi mikondo ya adani. Kukhulupirira Mulungu ndiye chishango ndi chitetezo ku ziwembu za mdiererekezi. M'mayeso, m'mayesero, m'mazunzo, ndi m'mavuto amtundu uliwonse, tiyeni tinyamule chishango cha chikhulupiriro ndi kusunga kudalira ndi kukhulupirira mwa Mulungu, chikondi chake ndiponso kupereka kwake.

Chisoti cha Chipulumutso: Chofunika kwambiri kuti munthu apulumuke pankhondo, chinali kuteteza mutu ndi nkhope ya msilikali. Chipulumutso ndi mphatso ya Mulungu ndipo mwa chisomo ndi mphamvu zake zokha tingathe kukhala ndi moyo wopambana. Tikapululumutsidwa, titha kukhala ndi moyo ndi chidaliro komanso chitsimikizo kuti ndife otetezedwa ndi kupatsidwa mphamvu ndi Mulungu. Sitalamuliridwanso ndi uchimo, thupi, kapena anthu otizungulira. Timatetezedwa ndi kusungidwa mwabwino pamene tidalira ntchito yaumulungu ya Mulungu.

Lupanga la Mzimu:

Lupanga linali chida choopsa chomwe chimagwiritsidwa ntchito polimbana ndi adani. Msilikali sayenera kuti nthawi zonse azikhala modzitetzeza koma adzipita kutsogolo, ndi kumagonjetsa. Mulungu adapereka Mzimu wake Woyera kuti upereke mphamvu kwa mwana wa Mulungu kuti athane ndi mdani ndikukuza malo amene iye akulamulira. Lupanga la Mzimu ndiwo "Mau a Mulungu"; ndi Baibulo ndi lolankhulidwa ndi Mzimu Woyera. Zimatipatsa mphamvu kuti tigonjetse mdani monga mmene Yesu anachitira pamene anagwiritsa ntchito Malemba kuti agonjetse mdiererekezi m'chipululu muja.

Mulungu sanatitumize kuti tikhale oyera ngati Khristu popanda kutipatsa zonse zomwe tingathe kuti tigonjetse mphamvu ya mdani. Dzikonzekeretseni, osati ndi malingaliro ndi nzeru za dziko, osati ndi ziphunzitsa za magulu achipembedzo, koma ndi zida za Mulungu. Ogonjetsedwa, obwerera m'mbuyo, amene avulazidwa ndi uchimo ndi mphamvu za thupi akhoza kuukanso ndi kukhala ndi moyo wachipambano ndi mphamvu ya Mulungu. Pali chiyembekezo ndi chipambano chodabwitsa! ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org



Mau a Mkonzi



Kukawatsegulira maso ao, kuti atembenuke kuchokera kumdima, kulinga kukuunika, ndi kuchokera ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu, kuti alandire iwo chikhululukiro cha machimo, ndi cholowa mwa iwo akuyeretsedwa ndi chikhulupiriro cha mwa Ine. — Machitidwe 26:18

Panjira yopita ku Damasiko, Yesu anaonekera kwa Saulo. Sauloyo anafunsa kuti, “Ndinu yani Mbuye?” Yesu anayankha kuti, “Ine ndine Yesu” (Machitidwe 26:15). Kenako Yesu anapitiriza kufotokoza za maitanidwe ake aumulungu ndi dongosolo lake kwa Saulo. Iye amayenera kukalalikira uthenga wabwino wakuti maso a anthu atseguke ‘kuchokera ku ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu’, Aleluya! Umenewo ndiye uthenga wabwino mpaka lero lino. Mphamvu ya Satana yathyoledwa; pali chiwombolo ndi chigonjetso kwa wochimwa ndi kwa wobwerera m’mbuyo.

Ndi misozi komanso chisangalalo chachikulu, ndikulemba kalata iyi ya Uthenga Wabwino wa Choonadi pa mutu wa moyo wa Chikhristu wopambana. Anthu ambiri akupitiriza kukhala mu uchimo ndipo akuyesera kuti asiye mchitidwe uwu wauchimo. Pamene akulimbana ndi kulephera, kugonjetsedwa ndi zizolowezi ndi thupi, chikhulupiriro chawo chikuwonongeka. Ambiri sakhulupiriranso kuti munthu akhoza kukumana ndi chipulumutso. Musangalale nane pamene mukuwerenga kalatayi. Kukadalipo kuwomboledwa ku uchimo komanso mphamvu yokana mayesero. Mulungu angathe, adzatero, ndipo akusinthabe miyoyo.

Talingalirani ndime zimene zili mu mau odabwitsa a nyimboyi, *Muli mphamvu m’mwazi wake yolembedwa* ndi Lewis E. Jones.

Ufuna kuomboledwa kodi?
Ilipo mphamvu m’mwazi wake;
Ufuna kugonjetsa zoipa?
Muli mphamvu m’mwazi wake.

Korasi:
Muli mphamvu, mphamvu, mphamvu yodabwitsa
M’mwazi wa Yesuyo;
Muli mphamvu, mphamvu, mphamvu yodabwitsa
M’mwazi wa Mwanawankhosa.

Sitiyeneranso kugwadira ndi kutumikira uchimo koma tikhala mu ufulu kudzera mu mphamvu ya mwazi. Ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha zimenezo zinandichitikira. Nyimbo ina yotchuka imati, “Ine ndine wochimwa chabe, koma wopulumutsidwa mwa chisomo.” Ndimayamika Ambuye chomwe sichiri chondichitikira. NDINALI wochimwa koma sindilinso chifukwa Yesu anandikweza ndi kundichotsa mu uchimo.

Dongosolo la Mulungu ndi labwino komanso lokwanira. Ngati munthu sakukhala m’moyo wa chipambano, ndiye kuti akusowekera mphamvu ya Mulungu. Anthu ambiri amabwerera mu uchimo chifukwa amalephera kufunafuna Mulungu kuti awadzaze ndi Mzimu Woyera. Ndikukhulupirira kuti ichi ndi chim odzi mwa zofunika kwambiri pakati pa Akhristu masiku ano. Anthu ayenera kupatulira miyoyo yawo mokwanira pa guwa la nsembe ndi kudzazidwa ndi moto ndi mphamvu ya Mzimu Woyera. Mphamvu ya Mzimu Woyera yokhazikika ndi yofananiza ndi imene imathandiza mkhristu kukhala ndi moyo wokondweretsa Ambuye watsiku ndi tsiku. Zimenezi zimalimbana ndi kukonzanso moyo wosakhazikika ndi wosadalirika umene anthu ambiri akukhalamo.

Ambuye akudalitseni pamene mukuphunzira zamulungu zokhudza chiphunzitsochi, ndipo koposa zonse, kuti mulimbikitsidwe ndi kutsutsidwa pamene mukutsegula mtima wanu kuti mukhale ndi moyo wachigonjetso.

Michael W. Smith

April 2023



Mukafuna kutipeza


pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.





Kalozera posanthula Baibulo

Mutu: Moyo Wachikristu wopambana

Kuwerenga Malemba: *Koma ayamikike Mulungu, amene atipatsa ife chigonjetso mwa Ambuye wathu Yesu Khristu. — 1 Akorinto 15:57*

Mwachidule: Pali zochitika zomwe zimapezeka kudzera mu dongosolo la Mulungu la chipulumutso kuti tikhale ndi moyo wosasintha, wachigonjetso pa uchimo ndi dziko lapansi.

I. Kumasuka ku uchimo

- A. Aroma 6:1-2 Kodi tidzapitirizabe kuchimwa?
- B. Aroma 8:3 Chimene lamulo silinakwanitse kuchita.
- C. Mateyu 1:21 Yesu amapulumutsa ku uchimo.
- D. 2 Akorinto 5:17 Zinthu zakale zapita.
- E. Aroma 6:6-7 Kumasulidwa ku uchimo.

II. Mphamvu yokhala ndi moyo wopanda uchimo

- A. 1 Yohane 1:7 Kuyeretsedwa ku uchimo onse.
- B. 1 Yohane 3:6-8 Uchimo ndi wa mdierekezi.
- C. 1 Yohane 5:18 Wobadwa mwa Mulungu.
- D. Aroma 6:12-14 Uchimo sudzakhala ndi ulamuliro.
- E. 1 Akorinto 6:9-11 Tsopano tili wolungama.

III. Malangizo akuti tisachimwe

- A. Yoh 8:11 Pitani, ndipo musakachimwenso.
- B. 1 Akorinto 15:34 Musachimwe. (1 Yohane 2:1)
- C. (Tito 2:11-12) Kanani kusapembedza/khalani mwaumulungu.
- D. 1 Petro 2:21-22 Tsatirani chitsanzo cha Khristu: opanda uchimo.

IV. Mphamvu ya Mzimu

- A. Luk 24:49 Wodzazidwa ndi mphamvu.
- B. Machitidwe 1:8 Mzimu Woyera amapereka mphamvu.
- C. Yohane 14:26 Mzimu amatonthoza ndi kuphunzitsa.
- D. Zekariya 4:6 Kupambana mwa Mzimu wa Mulungu.

V. Malonjezo a Mulungu

- A. Yoh 8:36 Mudzakhala mfulu ndithu.
- B. 1 Yohane 5:4-5 Chipambano chimene chimaligonjetsa dziko lapansi.
- C. Luk 10:17 Ziwanda zimagonjera.
- D. 1 Akorinto 10:13 Pewani mayesero.
- E. Salmo 44:3 Kupambana ndi dzanja la Mulungu.
- F. Afilipi 4:13 Zinthu zonse mwa Khristu.
- G. Deuteronomo 20:4 Mulungu adzakumenyerani nkondo.
- H. 1 Yohane 4:4 Wamkulu ndi Iye.
- I. Yohane 16:33 Khristu waligonjetsa dziko lapansi.

Kumaliza

Koma m'zonsezi, ife tilakatu, mwa Iye amene anatikonda. — Aroma 8:37

Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu

amauza anthu kuti

“PITANI NDIPO MUSAKACHIMWENSO”

Ngati moyo wopanda uchimo

unali wosatheka?

MOYO WACHIKHRISTU WOPAMBANA



“Mau a Mulungu amanena momveka bwino kuti: “Ndipo mwazi wa Yesu Mwana wake utisambitsa kutichotsera uchimo wonse.”

Kodi tipitirizebe kuchimwa? Kodi tiyenera kugonjera ku mayeso za Mdierekezi? Kodi tiyenera kukhalabeA m'moyo wolephera nthawi zonse ndi kugonjetsedwa mu zochitika zathu zachikhristu? AYI! Tiyamike Mulungu popeza pali chipambano ndi mphamvu yakugonjetsa kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

Chipulumutso ku tchimo

Mtumwi Paulo anafunsa funso lomweli pa Aroma 6:1-2, “Tidzakhalabe mu uchimo kodi, kuti chisomo chichuluke? Msatero ai.” Akhristu ambiri amati TIYENERA kuchimwa mochulukira kapena mocheperapo tsiku lililonse. Iwo amachepetsa nsembe ya Khristu kuti ili chisomo cha kukhulukira koma amalephera kuvomereza chisomo cha chiombolo chimene chimakweza anthu ochimwa kuchoka ku machimo awo kupita ku chikhaliidwe cha chigonjetso kupyolera mu mphamvu ya mwazi. “Zimene lamulo silinathe kuchita, popeza linafoka mwa thupi, Mulungu anatumiza Mwana wake wa Iye yekha m'chifanizo cha thupi lauchimo, ndi chifukwa cha uchimo, natsutsa uchimo m'thupi” (Aroma 8:3). M'nyengo ya Chilamulo, anthu sankatha kukhala opanda uchimo—zikhaliidwe zopotoka zimene zimalekanitsa munthu ndi Mulungu. Yesu anabwera kudzachita zimene Chilamulo sichikanatha kuchita. Dzina lake lenilenilo limalankhula za dongosolo loona la chipulumutso, “Pakuti adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo” (Mateyu 1:21).

Pali chiwombolo

Aphunzitsi onyenga ndi ziphunzitso zina amachepetsa dongosolo laulemerero la chipulumutsoli kuti likuimira Khristu kupulumutsa anthu ake MU machimo awo. Mdierekezi ndi amithenga ake ndiwo amene amafalitsa chiphunzitso chonyenga kuti abe chiyembekezo chenicheni ndi chimwemwe cha chipulumutso choona. Mulungu alemekezeke, kuti tikhoza kupulumutsidwa ku mphamvu ya uchimo kuti tiyende mu chilungamo ndi chiyero. Malemba amaphunzitsa momveka bwino za moyo

wachigonjetso ndi kumasulidwa ku ukapolo. “Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano” (2 Akorinto 5:17). Makhalidwe akale, zizolowezi, zilakolako, kuwawidwa mtima, zonse zimene zimawagwira anthu mu uchimo zimathyoledwa ndi mphamvu ya Mulungu. Tchimo limawonongedwa ndi kugonjetsedwa kuti “tisakhalenso akapolo a uchimo” (Aroma 6:6). Mkhristu angathe ndipo ayenera kukhala ndi moyo wachigonjetso pa uchimo ndi ukapolo wake. Ngakhale mphamvu ya uchimo ndi yayikulu motani, pali chiwombolo mu chipulumutso.

Moyo wosinthidwa

Paulo anavomereza za tchimo lakale la otembenuka mtima pa 1 Akorinto 6:9-11. Ena anali adama, opembedza mafano, achigololo, ogonana amuna kapena akazi okhaokha, akuba, zidakwa, ndi zina zotero. “Ndipo ena a inu munali otere; koma munasambitsidwa, koma munayeretsedwa, koma munayesedwa olungama, m'dzina la Ambuye Yesu Khristu, ndi mwa Mzimu wa Mulungu wathu.” Palibe wochimwa amene adzalandire ufumu wa Mulungu. Onse anachimwa, komabe miyoyo imasinthidwa ndi makonzedwe a Mulungu. Mphamvu ya mwazi wa Yesu ndi yoposa mphamvu ya uchimo. Zikhoza kukhala zomvetsa chisoni kuti odzitcha Akhristu ambiri sanapeze chipulumutso chenicheni. Chipulumutso chidzasintha kwambiri moyo ndikupangitsa munthu kugonjetsa uchimo wonse mwa chisomo cha Mulungu! Mau a Mulungu amanena momveka bwino kuti: “Ndipo mwazi wa Yesu Mwana wake utisambitsa kutichotsera uchimo wonse” (1 Yohane 1:7).

(Yapitirira pa tsamba 6)

Musachimwe

Tchimo ndi zotsatira za chikoka ndi mphamvu ya mdierekezi. Yesu anabwera padziko lino lapansi ndipo anafa kuti “akaononge ntchito za mdierekezi” (1 Yohane 3:8). Vesi 6 imati, “Aliyense wokhala mwa iye sachimwa...Iye wochita tchimo ali wochokera mwa mdierekezi.” Mtumwi akulengezanso mu 1 Yohane 5:18 kuti, “Tidziwa kuti yense wobadwa kuchokera mwa Mulungu sachimwa...ndipo woipayo samkhudza” Dziko lonse lapansi limve ndi kudziwa kuti m’badwo uno muli moyo womasuka ku uchimo ndipo mphamvu ya Satana yathyoledwa kudzera mwa Khristu. “Uchimo sudzachita ufumu pa inu; pakuti simuli omvera lamulo, koma a chisomo” (Aroma 6:14). Chimene kale chinkalamulira ndi kuongolera khalidwe la uchimo panso pa lamulo chaphwanyidwa ndi mphamvu yopulumutsa ya chisomo.



Chisomo cha Mulungu chimathandiza kukhala opanda tchimo

Ngakhale akatswiri a zaumulungu amatha kupotoza ndi kuyesetsa

“Mzimu Woyera amapereka mphamvu kwa Mkhristu kunena mosalekeza kuti “ayi” kwa mdierekezi, “ayi” kwa thupi, “ayi” ku dziko lapansi, ndi mphamvu ya kunena kuti “eya” kwa Ambuye.”

kuti tchimo silolakwika, Mau a Mulungu amaphunzitsa moyo wa chigonjetso chenicheni pa uchimo. Yesu mwini anauza mkazi wa chigololo, “Pita, ndipo usachimwenso” (Yohane 8:11). Yesuyo sanamulangize kuti achite zinthu zimene maiyo sakanakwanitsa koma anali kumupatsa chiyembekezo ndi mphamvu kuti apite ndi kukakhala popanda nsinga za mchitidwe wa chigololo. Paulo anapereka malangizo ofanana nawo pa 1 Akorinto 15:34 kuti, “Dzukanani m’chilungamo, ndipo musachimwe.” Petro akutilimbikitsa pa 1 Petro 2:21-22 kuti titsatire mapazi

a Khristu amene “sanachimwe.” Zoonadi, chisomo cha Mulungu chimene chinabweretsa chipulumutso chimatiphunzitsa, “kuti tikane chisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo wodziletsa, wolungama, ndi wopembedza, m’dziko lino lapansi” (Tito 2:11-12). Uwu ndiwo moyo wopambana!

Chipulumutso chathunthu

Chipulumutso ndi chochitika chodabwitsa chimene wochimwa amakhulupirira mwa Khristu, kulapa ku machimo, ndi kukhululukidwa ndi kuyeretsedwa ndi mwazi wa Yesu. Chotengeracho chimakhala choyera, koma Mulungu akufuna kuchidzadzaza ndi Mzimu Wake Woyera. Yesu anauza ophunzira ake kuti: “Khalani inu mumzinda wa Yerusalemu, kufikira mudzavekedwa ndi mphamvu yochochera kumwamba” (Luka 24:49). Chimodzimodzinso, pa Machitidwe 1:8 amanena kuti, “Mudzalandira

mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu.” Ichi ndi chinthu chofunikira komanso chothandizira kukhala ndi moyo wopambana. Kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi gawo lofunikira la dongosolo lathunthu la chipulumutso. Mzimu Woyera amapereka mphamvu kwa Mkhristu kunena mosalekeza kuti “ayi” kwa mdierekezi, “ayi” kwa thupi, “ayi” ku dziko lapansi, ndi mphamvu ya kunena kuti “eya” kwa Ambuye. Mzimu Woyera amatonthoza, kuphunzitsa, kutsogolera, ndi kupereka mphamvu (Yohane 14:26). Mzimu Woyera wokhala mwa wokhulupirira adzapereka mphamvu mu kufooka ndipo adzalimbitsa thupi kuti chigonjetso ndi chiyero zisungidwe.

Malonjezo kwa okhulupirira

Mau a Mulungu ndi odzaza ndi malonjezo amene amalimbikitsa ana a Mulungu pamene akukumana ndi dziko lamdima. Kumasuka ku uchimo sikuyenera kungokhala kwakanthawi, chifukwa lonjezo laperekedwa kuti, “Chifukwa chake ngati Mwana adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu.” (Yohane 8:36).

Tikhoza kulimbika mtima pakuti, “Pakuti chilichonse chabadwa mwa Mulungu chiligonjetsa dziko lapansi” (1 Yohane 5:4-5). Moyu wa Mkhristu suli wogonjetsedwa ndipo sumazingidwa ndi kulephera; koma umadziwika ndi chigonjetso, mphamvu ndi kukula. Sitiyenera kuopa Satana akakwiya ndi kubangula, pakuti ngakhale ziwanda zimatigonjera m’dzina la Yesu (Luka 10:17). Pamene mayesero ali amphamvu ndipo zikuoneka kuti palibe njira yotulukira, Mulungu walonjeza kuti “adzaikanso populumukirapo, kuti mudzakhoze kupirirako” (1 Akorinto 10:13). Nthawi zina thupi limakhala lofooka ndipo mphamvu ya mdani imakhala yamphamvu. Komabe, tikakhala okonzeka ndi zida za Mulungu, tingadalire mphamvu zake kuti atichitire zimene sitingathe kudzichitira tokha.

Ana a Israele sanagonjetse Kanani ndi lupanga lawo koma ndi dzanja lamanja ndi mkono wa Mulungu (Salmo 44:3). Mulungu adzamenyera nkondo ana ake (Deuteronomo 20:4) ndi kuwasunga mpaka mapeto. Tikhoza kunena malonjezo a Mulungu ndi kunena pamodzi ndi Paulo kuti: “Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo” (Afilipi 4:13). Limbikitsani ndi kufunafuna ndi kukhala moyo umenewo wa chigonjetso mosasamala kanthu za mikhaliidwe ndi malingaliro, pakuti “Iye wakukhala mwa inu aposa iye wakukhala m’dziko lapansi” (1 Yohane 4:4).

Yesu anadziwa kuti dziko linali lamdima ndi kuti munali kulimbana mkati ndi kunjira, koma Iye, monga wopereka mtendere ndi chipambano, akutilimbikitsabe lero lino kuti: “M’dziko lapansi mudzakhala nacho chivuto, koma limbikani mtima; ndalingonjetsa dziko lapansi Ine” (Yohane 16:33). Pali mtendere, chigonjetso, ndi mphamvu pa uchimo wonse, ndipo titha kukhala moyo wachigonjetso tsiku ndi tsiku chifukwa “Ndife opambana ndi opambana mwa Iye amene adatikonda” (Aroma 8:37).

“Ambuye tithandizeni kuti tisakhale ndi mtima wogonja kapena kulephera, koma tiyeni tikweze mmwamba ndi mphamvu ya Yesu ndi Mzimu Woyera ndikudzitengera moyo wodabwitsa, wachigonjetso umene umapezeka mwa Inu nokha. Amen.” ■

Mafunso Mayankho



Kodi timatanthauza chiyani kwenikweni tikanena kuti kukhala “omasuka ku uchimo”?

Pamene munthu wapulumutsidwa, lemba limanena momveka bwino kuti pali mphamvu yokhala ndi moyo osachimwa. “Yense wobadwa kuchokera mwa Mulungu sachita tchimo” (1 Yohane 3:9). Anthu akamakambirana za tchimo, ndikofunikira kuzindikira ndi kumvetsetsa matanthauzo ake.

Chipangano Chatsopano chimapereka matanthauzo okwana anai a uchimo—zinthu zimene zimalekanitsa munthu ku chijanano chake ndi Mulungu. Mwana weniweni wa Mulungu amakhala osaphwanya malembawa.

“Chosalungama chilichonse chili uchimo” (1 Yohane 5:17).

“Ndipo tchimo ndilo kusaweruzika.” (1 Yohane 3:4).

“Potero kwa iye amene adziwa kuchita bwino, ndipo sachita, kwa iye kuli tchimo” (Yakobo 4:17).

“Chinthu chilichonse chosatuluka m’chikhulupiriro, ndicho uchimo” (Aroma 14:23).

Kuti timveke zimveke bwino, Lamulo la Mose linali ngati “namkungwi wathu wakutifikitsa kwa Khristu” (Agalatiya 3:24). Anthu pansi pa lamulo sakanatha kukhalabe ndi moyo wachipambano popanda kuchimwa. Talingalirani za Davide amene anachita chigololo komanso Abrahamu amene ananena bodza. Mitima yawo imafuna itatumikira Mulungu, koma analibe mphamvu yakukhalabe ndi moyo wopanda uchimo; chotero anadalira nsembe za nyama molingana ndi lamulo la Mulungu kuti akhululukidwe. Pansi pa Pangano Latsopano, muli mphamvu m’mwazi osati kungokhululukidwa kokha koma kuti “tipite ndi kusakachimwanso.” Lamulo linaperekedwa ndi Mulungu kuti liwulule uchimo kuti potero timvetsetse ndi kudziwa kuti sitingapitire kukhala osachimwa mwa kuthekera kwathu. “Pakuti uchimo udziwika ndi lamulo” (Aroma 3:20).

M’Chipangano Chatsopano, uchimo ndi nkhani ya mumtima ndipo ndi kupandukira Mulungu ndi njira yake, popeza kudzera mwa Khristu TIKHOZA kukhala ndi moyo popanda kuphwanya malamulo. Nkofunika kuidziwa kuti pamene Paulo ndi Yohane akulankhula za anthu amene sadzakalowa Kumwamba, iwo anatchula zinthu zodziwika bwino monga izi - kupembedza mafano, dama, chigololo, bodza, kuba, kuledzera, ndi zina zotero. Zinthu izi zili ngati MAKHALIDWE olakwika amene amasiyanitsa munthu ndi Mulungu, Awa ndi machimo.

Kodi kukhala ndi moyo wopambana wopanda uchimo kumatanthauza kuti sindidzalakwa kapena kulephera?

Ili ndi funso lofunika kwambiri pamutu womwe tikukambiranawu. Sindinakumanebe ndi Mkhristu yemwe ndi wopulumutsidwa ndi wodzazidwa ndi Mzimu Woyera koma sanalepherepo kapena kulakwitsa. Komabe, pali kusiyana pakati pa tchimo ndi kuperewera pa ungwiro wa chisomo. Akhristu ayenera kukonda Mulungu kuposa china chilichonse ndipo cholinga chawo komanso khumbo lawo liyenera kufuna kukhala ngati Khristu. Izi sizikutanthauza kuti ndife angwiro mwaumunthu. Sikuti sitimachita makhalidwe olakwika omwe amatisiyanitsa ndi Mulungu, koma pali magawo ena amene tikuyenera kukula. Ngati tikufuna kukula, ndiye kuti pali zina zoperewera. Nthawi zambiri zoperewerazo zimawululidwa kudzera mu zolakwika ndi zolephera.

Mwachitsanzo, Mkhristu sangayankhe ndi chimwemwe chokwanira kapena kuleza mtima pamene wakhumudwitsidwa. Uku ndikulephera kapena kulakwitsa. Mkhristu weniweni sangapeze chonamizira koma adzafunafuna Ambuye kuti akule ku gawo limenelo la moyo. Mwana wa Mulungu sadziwika ndi kulephera kwake koma makamaka ndi kupambana kwake. Chinthucho chitha kukhala uchimo ngati munthuyo aganiza kuti avomereza kulephera kukhala umunthu wake wauzimu ndikukhazikika pachisomo chochepa.

2 Petro 3:18 amatiphunzitsa kuti, “kulani m’chisomo” ndipo 2 Petro 1:5 amatilangiza kuti “muonjezerapo ukoma pa chikhulupiriro chanu, ndi paukoma chizindikiritso...” Pali kukula mu moyo wachikhristu, ndipo tikatumikira Ambuye kwa nthawi yaitali, tiyenera kukhala ngati Khristu. Utumiki unaikidwa mu thupi kuti “akonzere oyera mtima” (Aefeso 4:12). Chifukwa chake, Mkhristu ali ndi magawo amene akhoza kukula ndi kukhala wangwiro mwa Khristu.

Ana a Israele anakumana ndi nkondo zambiri ku Kanani. Pamene anadzipereka kwa Mulungu, adapambana ndi kugonjetsa kwamphamvu. M’dzikomo munali mizinda ya ziphona komanso makoma ataliatali, komabe iwo anapambana ndi mphamvu ya Mulungu chifukwa anali omvera.

Utumiki wa Probe Ministries udatulutsa zotsatira za kafukufuku wao amene anapanga mu chaka cha 2020 pakati pa anthu a ku America okwana 3,106 a zaka za 18 mpaka 55.

- Kupitirira 60% ya achinyamata achikhristu (18-39) amakhulupirira kuti Yesu, Buddha, ndi Muhammad onse ali ofanana pamene tikukamba za njira ya chipulumutso.
- 30% ya Apulotesitanti obadwanso mwatsopano adavomereza kapena samatsimikiza ngati Yesu adachimwako pamene anali padziko lapansi.
- Pafupifupi 80% ya achinyamata achikatolika sadziwa ngati Yesu anakhala moyo wopanda uchimo padziko lapansi.



**Mau a
Nyengo
Yake**

PAMENE CHIKHULUPIRO CHIKUGWEZEKA

Ndipo pomwepo Yesu anatansa dzanja lake, namgwira iye. — Mateyu 14:31

Pamene ngalawayo inkagwedezeka ndi mafunde ndi kuwomba mphepo mundima wa usiku, Yesu anadza akuyenda pamadzi. Ophunzirawo anachita mantha poganiza kuti mwina ndi muzukwa. Yesu analankhula nawauza kuti: “Limbani mtima; ndine; musawope” (Mateyu 14:27). Ndi mwai waukulu kwambiri kumva mau a Mpulumutsi mu mikuntho yovuta ya moyo. Kukhalapo kwake ndi mau ake zikulowabe m’mikuntho lerolino.

Petro anafuna kutuluka pamadzi kwa Khristu. Yesu anamuza iye kuti abwere; ndipo kotero, pakati pa namondwe, Petro anatuluka m’ngalawa. Chikhulupiriro ndi kudalira koposa. Petro anayenda pamadzi kupita kwa Yesu. Ichi chinali chionetsero chachikulu chakuthupi cha chigonjetso chomwe chili mwa Khristu! Petro anatha kugonjetsa chilengedwe cha madzi ndi mphamvu ya Mulungu. Chipulumutso ndi chofanana ndi chakuti timatha kugonjetsa chibadwa chathu chofuna kuchimwa ndikukhala moyo wachiyero ndi mphamvu ya Mulungu.



Pamene Petro ankayenda pamadzi, anayang’ana uku ndi uku n’kuona kuopisa kwa chimphepocho. Kuopisa kwa mafundewo kunachititsa kuti chikhulupiriro chake chigwedezeke, ndipo anayamba kumira. Asanamire, iye analirira kwa Yehova. “Nthawi yomweyo Yesu anatambasula dzanja lake namgwira,” namudzuzula chifukwa cha kupanda chikhulupiriro kwake. Pamene anabwerera m’ngalawamo, namondweyo analeka.

Kupambana ndi kodabwitsa! Ndi mdalitso wozizwitsa pamene tiona mphamvu ya Mulungu imene imatithandiza kugonjetsa uchimo ndi dziko lapansi. Komabe, pali nthawi zina pamene mphepo yamkuntho imatha kukhala yoopsa kwambiri; Ngati sitisamala, chikhulupiriro chathu chingayambenso kufooka. Sitiyenera kumira ngati tiyang’ana pa Yesu. Ngati tipeza chikhulupiriro chathu chikugwedezeka pamene mphamvu za dziko lapansi ndi za thupi ziyamba kukoka molimba, tikhoza kulira kwa Yehova ndipo adzatikweza; ndiye Mpulumutsi wathu wachikondi.

Mmene Yehova akutansa dzanja lake kwa ife pamene chikhulupiriro chathu chayamba kufooka, kodi sitingachitenso zokhala ngati zomwezo kwa mbale kapena mlongo mnzathu mwa Ambuye? ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE